

1 Timoteo : Mau otsogolera

Mutu : Mau otsogolera bukuli

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero tiyambe ndi mau apa Ezekieli 33:4, amene akuti, “Ndipo wina kumva adamva mau a lipenga, koma osalabadira, likudza lupanga, nilimchotsa, wadziphetsa ndi mtima wake.”

Lero tikulowa m’Chipangano Chatsopano m’buku la kalata ya 1 Timoteo. Iyi, ndi kalata yomwe ikutitsogoleraife ku makalataangapo amene analembedwa ndi Paulo. Pali makalata atatu amene alimgulu limodzi. Awa, ndi makala a 1 ndi 2 Timoteo komanso Tito. Makalataamenewa akupereka uphungukwa atsogoleri a mipingo pankhani zokhudzakayendetsedwekamipingo wamba (Pastoral letters). Tikunena kuti mipingo wamba chifukwa makalata awa, sakukamba za mpingo ngati thupi limodzi la Kristu padziko lonse lapansi ayi. Kutanthauza kuti makalata awa sakukamba za mpingo womwe suoneka ndi maso ayi. Koma m’makalata awa,

akukamba za kayendetsedweka mpingo womwe ndi kaguluka anthuokhulupirira m'dera limodzi.

Ndiye makalata awa, analembedwakwaalalikiachinyamata awiri, amene anaitumikira pamodzi ndi Paulo; iwowa ndi Timoteo ndi Tito.

Awa, ndi atumiki amene ali amodzi mwa anthu amene anadziwa Kristu kapena kuti anatembenuka mtima mu utumiki wa Paulo.

Mwanjira ina atumiki awiriwa anali zipatso za utumiki wa Paulo, amene akhala akuthandizira mu utumiki wa Paulo. Tere, m'makalata awa, Paulo akupereka malangizo pakayendetsedweka mpingo (umene ndi gulu la anthu pamalo amodzi).

Tsono pali umboni waukulu wakuti makalata awa, analembedwa ndi Paulo pamene anaturukaundende wake, woyamba pakati pa zaka za 60-62 A.D. Apa, ndipamene anayamba ulendo wake wachinayiwoyenderamipingo. Ndiye paulendo umenewu, ndipo pamene anapereka udindo kwa Tito, kuti akhalire pa Krete monga womuimira iye komanso anasiya Timoteo ngati woyang'anira mpingo wa Efeso. Iyi, ndiyo nthawi yomwe iye, anapitilira ku Filipi, ku Makedoniya, kumpoto kwa Greece. Uku, ndikumene anakalemberekalata yoyamba kwa Timoteo ndikalataina kwa Tito

pakati pa zaka za 63-65 A.D. Ndiye patapita nthawi ndi momwe anapitilizaulendo wake wa ku Roma, komwe anakamangidwa kachiwiri. Uku, ndikumene anakapeza mwayi wolembe kalatayachiwiri yopitakwa Timoteo patatsala nthawi pang'ono kuti amunyonge pakati pa zaka za 67/68 A.D.

Tsono Paulo m'makalataatatuwa akufotokonzamo zinthu ziwiri; zomwe ndi chikhulupiriro cha mpingo komanso momwe mpingo uyenera kukhalira. Kutanthauza kuti mpingo m'kapembedzedweka mkati mwake kakhale koyenera ndipo kunja kwake ndiko kumene kuonetse ntchito zabwino. Mwanjira ina Paulo akulangiza kuti, kupembedza uyenera kukhala kochokera mumtima, pamene ntchito ziyenera kuonetsedwa kunja kapena kubwalo kwa mpingo.

Paulo, m'makalataatatuwa, akuyika maso ake kwambiri pa mitu iwiri. Taonani m'l Timoteo 1, akukamba za chikhulupiriro cha mpingo, kunena za chikhulupiriro chimene mpingowoumatsamirapo (doctrine). Pamene tilowa m'chapter 2, ndi momwe tipeza nkhani yakayendetsedweka mpingo. M'chapter 3, akukamba za adindo mumpingo. Pamene m'chapter 4, Paulo akukamba za chiphunzitso chonama chomwe chikudza ndipo mu

chapter 5 ndi 6, Paulo akukamba za ntchito za adindo mu mpingomo.

Tsono tikalowa mu 2 Timoteo 1, Paulo akukamba za zosautsa zomwe mpingo umakumananazo ndipo m'chapter 2, ndimomwe akufotokonza za ntchito zomwe mpingo uyenera kugwira. Ndiye mu chapter 3 ndi 4, ndimomwe Paulo akulemba za kuchoka pachikhulupiriro ndi kukhala wokhulupirika mumpingo.

Ndiye Tikaonanso m'kalatayolemba Tito, chapter 1, Paulo akufotokonza za ndondomeko yoyendetsera mpingo, pamene chapter 2, ikufotokonza za chikhulupiriro chomwe mpingo umakhazikitsidwirapo. Pamene chapter 3, muli ntchito zoyenera mpingo. Kutsimikiza ganizo lakuti, chipembedzo chiyenera kukhala mkati, pamene ntchito ndizo ziyenera kuonekera kunja.

Tsono masiku ano timapeza chizindikiro choyamba cha kukhazikitsidwa kwa mpingo, ndicho kumanga nyumba momwe wokhulupirirawo amasonkhanamo. Koma m'nthawi ya Paulo, sanali kukhazikitsa mpingo mwachizindikiro cha nyumba ayi, popeza iwowa amasonkhana m'nyumba za anthu wokhulupirirawo. Mwanjira ina tikunena kuti nyumba yopemphereramo m'nthawi

imeneyo, siinali yofunika kwambiri, kotero kuti nthawi zina amasonkhana m'nyumba zophunziriramo ana. Paulo amakonda kugwiritsa ntchito malo otere pamasana pamene anthu anali kupumira ku ntchito zawo. Tere, umu ndimomwe mpingo wa ku Efesounayambira.

Tsono Paulo anaika ndondomeko yakuti mpingo ukhazikitsidwe, kotero kuti mpingowoumayenerakudziwika kapena kukhala ndi zinthu zina zoyenereza. Poyamba anatsindika kuti mpingo uyenera kukhazikitsidwa ngati uli ndi chiphunzitso cha chikhulupiriro choyenera komanso chokwanira (doctrine). Iyi, ndiyo nkhani yomwe Paulo anali kulemba mpingo wa ku Efeso, yomwe ili pa 2 Timoteo 1:3, pamene akunena kuti, “Monga ndinakudandaulira iwe utsatirem’Efeso, popita ine ku Makedoniya, nditeronso, kuti ukalamulire ena ajawaasaphunzitse kanthu kena.” Kutsimikiza ganizo lakuti mpingo uyenera kukhala ndi kumangiririka pa chiphunzitso choyenera, osati kungodalira kapena kuika maso pa kumanga nyumba yosonkhaniramo ayi. Komanso taonani kuti Paulo pa 1 Timoteo 3:15, akuturutsa ganizo lina kwamnyamata wake Timoteo. Iye, akunena kuti, “Kuti udziwekuyenedwa kwake

pokhala m'nyumba ya Mulungu, ndiye Eklesia wa Mulungu wamoyo, mzati ndi mchirikizo wa choonadi.” Ndiye kuti nkhani iyi, imveke bwino, ndifuna ndiyambe ndi mau akuti, mpingo ndilo gulu la anthu wokhulupirira, amene ali thupi la Kristu pamalo ena. Ndiye kuti kagulu aka,ka wokhulupirira, kuti kayambe kugwira ntchito bwino pamalopo, payenera kukhala munthu wina amene aziyang'anirapamalopo, kumasesa, kaya kukolopa ndi kuonetsetsa kuti pamalopopakuoneka bwino komanso zinthu zonse ziri m'malo mwake.Ili, ndi ganizo lomwe likunena kuti, gulu lililonse pampingopo, liyenera kukhala ndi mtsogoleri wake monga pa choir, bungwe la maimbidwe, bungwe la chitukuko, bungwe lachipembedzo etc.Apa, Paulo akufuna kutsimikiza kuti anthu ayenera kukhala m'maudindo kuti mpingo uyendem'dongosolo labwino. Koma adindowo ayenera kukhala anthuamene ayenera kukwaniritsa zoyenereza zake.Kunena kuti mpingo uyenera kuyendetsedwa mwa ndondomeko yoyenera, pakuonetsa ntchito zabwino.Mwachisoni kuti ndondomeko iyi, siikutsatidwa chifukwa chakuti mipingo yambiri sikuonetsa zomwe iyenera kuchita.

Ndiye kuchokera m'makalata awa, mukuturuka njira zitatu zoyendetsera mpingo zomwe mipingoikulu-ikulu, yakhalaikugwiritsa ntchito. Koma ndiyenerakunenetsa kuti njira zitatu, ndizimene zakhala zikuutsa mkangano waukulu pakati pa mipingo. Tikunena kuti mipingoyakhalaikutsutsana kwambiri panjira momwe mpingo, uyenera kuyendetsedwera. Koma chinthu chochititsa chidwi ndi chakuti, njira zitatu zonsezi zikuturukam'makalata atatu omwewa.

Njira yoyamba yoyendetsera mpingo ndi ya Episcopal. Iyi, ndinjira momwe mumakhala munthu m'modzi kapena kaguluka anthu amene ali pamwamba pa mpingo. Munthu ameneyu, a mpingo wakatolikaamamutcha kuti "Papa." Pamene m'mipingoina amatchedwa Archbishop. Ndiye ngati palikaguluka anthu woyendetsam pingowo, kamatchedwa ma "bishop." Aka, ndi kayendetsedwekam'mpingowa ku Engaland m'mene anthu ochepa ndiwo amayendetsamipingo pakupereka malamulo ndi malangizo.

Njira yachiwiri ndiyo ya chi Presbyterian kapena mpingo woyendetsedwa ndi gulu loimira mpingo. Uwu, ndi mpingo womwe umasankhaakulua mpingo ndi atumiki kuti ndiwo ayendetse

mpingo wawo. Mwachisoni kuti panabukanso bungwe lina lalikulu lomwe limayendetsamipingoyo.

Ndiye njira yachitatu ndiyo yosiyana kwambiri ndi njira ziwiri tatchulazi. Iyi, ndi njira yotchedwa “Congregational”, momwe anthu a mpingo wonse pamodzi ndiwo amayendetsamipingowo. Njira iyi, ndiyimeneimagwiritsidwa ntchito m’mipingo ya Baptist.Kutanthauza kuti anthu a mumpingomo, ndiwo amapanga chiganizo mwanjira ya vote, monga pa ntchito zokhudza mpingo kapena kupatura anthu ena pamaudindo ena.

Wokondedwa anzanga apaulendo, mwina inu mwafunsa kale pamenepa kuti, zinatheka bwanji kuti kudzera m’makalata omwewa kuti muturuke njira zonsezi?Yankho likuti, zinatheka chifukwa cha katanthauzidwekamakalata amenewa.Ndiye tiyesetsa kuona katanthauzidwekamakalata amenewa.

Ndiye ndifuna ndiyambe ndimau ochititsa chidwi akuti, kale njira zitatu zonsezi zinali kuyenda bwino, masiku ano njira zomwezisizikuyenda bwino monga momwe zimayendera kale.Tsono pakafukufuku, panapezeka kuti m’kati mwanjira zimenezi, muli mikangano m’katimo, mwalowachisawawa ndi mkhalidwe

woukira.Ndiye tikafunsa tipeza kuti aliyense amanena kuti njira iyi, silibwino.

Ndiye chinthu china chomwe chikundichititsa chidwi ndi chakuti, kayendetsekaBomalathu, tinatsatira njira yoyendetsera mpingo. Taonani pomenyera ufulu wa dziko lino kuchoka m'manja mwa azungu, panali ganizo lakuti sikoyenera kuti munthu m'modzi (King/Queen) aziyendetsaBoma ayi. Kunena kuti anthu samafuna kuti munthu m'modzi kapena kaguluka anthu azilamulirazoyenerakuchiikta ayi.Apa, ndipamene panabwera ganizo lakuti mzika iliyonse yoyenera, iyenerakuvota. Kunena kuti munthu aliyense apereka maganizo ake pakayendetsedwekaBoma.Tsono mwina mukudabwa kuti, chifukwa chiyani anthu safuna kutsogoleredwa ndi munthu m'modzi kapena kaguluka anthu ochepa?Yankho likuti munthu alibe chikhulupiriro mwa munthu m'zake, kotero kuti sibwino kuika mphamvu m'dzanja la munthu m'modzi kapena kagulu kochepe ka anthu.Mwanjira akugwirizana ndi ganizo lakuti anthu ambiri sangalakwitse ayi.Apa, ndipamene panadza mau akuti, "Mau ya

anthu ambiri, ndiwo mau ya Mulungu.” Koma kunena mwachilungamo, izi sizoonayayi.

Ndikunena mau amenewa chifukwa tikaonetsetsa, tipeza kuti mipingo yathu siikuyendamonga momwe zinthu zimayenerakukhalira ayi. Ichi, ndichifukwa chakuti adindo amene akuyendetsamipingo, sakukwanira pa muyeso umene walembedwam’kalatayi. Tikunena kuti kalata iyi, yaperekazoyenerezamunthu kuti asenze udindo wa mumpingo. Taonani kuti zoyenereza zina zikunena kuti m’dindo akhale wosaledzera ndi wa mkazi m’modzi etc. Izi, ndizina mwa zinthu zofunika komanso zoyenereza munthu pa udindo wa mumpingo. Koma tikunena kutipali “Moyo wauzimu,” kuti ndicho chinthu chimodzi chimene ndichofunika kwambiri. Ndikunena kuti ichi, ndicho choyenereza kwambiri, chifukwa palibe njira iliyonse mwanjira zitatu zija, ingayende bwino pokhapokha anthu oyendetsawoali wolungama. Ngati moyo wawo sungalungamitsidwe ndi Kristu, ndiye kuti njira iliyonse kaya ikhala ya “Congregational, Episcopal kapena Presbyterian, siingakhale yothandiza ayi. Ili, ndibvuto lalikuru m’kayendetsedweka Bomalathu komanso

m'kayendetsedweka mpingo. Tikunena kuti ndikoyenera kusankha munthu amene akhoza kukwanitsa kuchita zomwe ziri mkayendetsedweka Boma kapena mpingo. Izi, ndizoyenereza zabwino, koma ndi kofunika kwambiri, kuona ngati munthuyuali mu wauzimu.

Tere, ndichifukwa chake Paulo m'kalata iyi, akuika mtima wake pa mau awiri okhudzauzimu wam'dindoyu. Iye, akunena kuti munthu wamoyo wauzimu ayenera kudziwikaza chikhulupiriro chake pa Yesu Kristu, ndipo ayenera kuyenda m'moyo wa chikondi. Kutsindika kunena kuti ngati m'dindosangaonetse zinthu ziwirizi, ndiye kuti sangathe kutumikira mumpingo, ngakhale atakhala ndi lusoloyenera.

Tsono mwina inu muli kakasi kuti izi, zitanthauza chiyani? Yankho likuti, ulamuliro omwe a dindoalinawo ndi si ulamuliro oyenera konse ayi, kotero kuti sayenera kudzimva kuti ali ndi ulamuliro chifukwa ulamuliro wonse wabwino uchokera kwa Yesu Kristu, amene ali mutu wa mpingo. Kunena kuti Mzimu Woyera ndiye ayenera kumatsogolera njira yoyenera kutenga ndi ntchito zofunika kuchita. Kutsindika kuti m'dindo sayenera kuikamo zokhumba

zake mu ntchito inailiyonse ayi. Kunena kuti m'dindoyu, ayenera kufufuza ndi kupeza chifuniro cha Mulungu. Apa, ndipamene tikunena kuti m'dindo ayenera kukhala wachikhulupiriro chokwanira kotero kuti adzafulumizidwa kuchita chifuniro cha Mulungu chifukwa cha chikondi chomwe alinacho pa Mulungu ndi pa anthu anzake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano tafika ndifuna tiimekaye, ndikufunsa inu amene munatenga udindo mumpingo kuti, kodi mulinazozoyenereza izi? Koma tiyenera kudziwa kuti ndikosatheka kuti m'dindoyense akondweretse munthu aliyense mumpingomo, tere udindo wake ndiwo kuonetsetsa kuti Kristu ndiye mutu wa mpingo. Mwachisoni lero lino alipo adindo ena, amene amaumitsa mitima yawo ndi cholinga chakuti aoneke ngati ndiwo auzimu. Iwo amakhala kuti alibe chidziwitso china chili chonse cha chifuniro cha Mulungu ndiye m'malo mwake amakwaniritsa zofuna zawo zimene amaganiza kuti ndizo zolungama.

Nkhani ikunenetsa kuti Kristu ndiye mutu wa mpingo wanu ndi wanga, ndipo ndifukwa chake Paulo akumutchula mu verse lachiwiri kuti ndiye “Ambuye wathu.” Kutsimikiza kuti ndiyekhayo

ayenera kukhala wotsogolapachinthu china chilichonse. Ndiye pamene tiwerenga Luka 6:46, Ambuye Yesu anadzudzula kuti, “Ndipo munditchuliranji Ine, Ambuye, Ambuye, ndi kusachita zimene ndizinena?” Ichi, ndichimene chili m’mpingo kuti muli akristu ambiri amene amanena kuti Ambuye, Ambuye, koma sakwanitsa kutsatira Iye. Tsono tikunenetsa kuti,kuti inu mukhale m’dindo mumpingo, muyenera kumachita chifuniro cha Kristu nthawi zonse, kumasunga malamulo ake ndi zokhumba zake popeza ndiye Mutu wa mpingo wanuwo.

Tsono pano sindifunakutsutsana ndi njira yoyendetsera mpingo wanu ayi, koma muyenera kudziwa kuti njira mukugwiritsantchitoyo, ikhoza kugwiritsidwa bwino ntchito ngati anthu alim’maudindomo ndiwo wotembenuka mtima. Kutsindika kunena kuti munthu waudindo, amene sadziwa Yesu, ndiye akhala ngati nyani amene watsakamira mu ntchito za mpingo.Ndiye ngakhale anthu ambiri amanena kuti ndintchito ya mpingo kukonzanso munthu wotere, koma chodziwika ndi chakuti pakali pano palibe umboni wochuluka wotere.

Ndiye tikunenetsa kuti 1 Timoteo, ndiyo kalata yomwe ikukhudza zinthu zofunika pakuyendetsa mpingo m'dera lathu, ndi chitsimikizo chogwiritsa ntchito adindo, amene angathe kuonetsa akutumikira mu mpingo wa Kristu kapena ayi. Tsono mwa zinthu zonse tanenazi, kodi inu mukupeza kuti mpingo wanu ndiwo mpingo wa Kristu?

Tiyeni tsono potsiriza tione ndondomeko ya mitu inam'kalatayi:

I. Kuona za chikhulupiriro cha mpingo, chapter 1

A. Mau otsogolera, chapter 1:1-2

B. Chenjezo kwa mipingo yomwe ili ndi ziphunzitso zosayenera, chapter 1:3-10

C. Umboni wa Paulo mwini, chapter 1:11-17

D. Udindo waperekedwa kwa Timoteo, chapter 1:18-20

II. Mapemphero a mpingo ndi udindo wa akazi mu mpingo, chapter 2

A. Mapemphero apa gulu ndi adindo oyenera pagulu la anthu, chapter 2:1-7

B. Kodi amuna apemphere motani? Chapter 2:8

C. Kodi akazi apemphere motani? Chapter 2:9-15

- III. Anthu oyenera kutumikira mu mpingo, chapter 3
 - A. Zoyenerezaakulu a mpingo, chapter 3:1-7
 - B. Zoyenereza atumiki a mpingo, chapter 3:8-13
 - C. Report la Paulo kwa Timoteo, chapter 3:14-16
- IV. Kutayika kwa chikhulupiriro (doctrine) mu mpingo, chapter 4
 - A. Kodi ma Apostle tingawadziwe bwanji? Chapter 4:1-5
 - B. Kodi “Mtumi wabwino” akhoza kuchita chiyani m’nthawi yakutayikakwa chikhulupiriro cha mpingo? Chapter 4:6-16
- V. Ntchito za adindoosiyana-siyana mu mpingo, chapters 5 ndi 6
 - A. Ubale wa m’busa ndi magulusiyana-siyana a mumpingomo, chapter 5,
 - B. Ubale wa wokhulupirira onse kwa wokhulupirira anzawo, chapter 6

Tsono ndi ndondomeko imeneyi, kwalerotilekeza pano.Koma timasanthula mau otsogolera m’kalata yoyamba ya Paulo yolembera mtumiki mnzake Timoteo.

Ambuye akuthandizeni pamene mulingalira za utsogoleri ndi njira yomwe mumayendetsera mpingo wanu. Amen!